NYA_HFT_SCRIPT _66

Program Name	**:**	**Chiyembekezo Changa**
Message Title	**:**	**Panalibetu Malo Akubisalapoa**
Duration	**:**	**15 Minutes**
Script Number	**:**	**066**
Presenter	**:**	

Utumiki wa Heralds of Hope ukupatsirani Program ya Chiyembekezo Changa!

Insert : **Signtune (6 secs)**
Presenter :

Okondedwa womvera program ya Chiyembekezo Changa amatipatsira ndi a Heralds of Hope. Umenewu ndi utumiki wapadziko lonse, umene cholinga chake ndi kufalitsa Uthenga Wabwino mu Chichewa, komanso muzilankhulo zina zikuluzikulu pano pa dziko lapansi zokwana 22.

Ndipo anthu zikwizikwi amamvera program imeneyi pofuna kudalitsika komanso kukula m'moyo wawo wa uzimu,

Ndine wokondwa kuti tili limodzi mu program ya lero. Kufalitsa uthenga kudzera pa wayilesi ndi gawo limodzi chabe mwa ntchito zambiri za utumiki wa Heralds of Hope.

Utumiki umenewu umaperekanso ma Baibulo ndi zowerenga zina, malinga ndi ndemanga yogwira mtima kwa munthu wamphumi, pa zomwe mwaphunzira mu program. Pamene utumiki wa Heralds of Hope ukumka nukulirabe, zinthu zambiri zikusintha. Koma chinthu chimodzi chimene sitikusintha ndicho kudzipereka kwathu pakuphunzitsa mawu a Mulungu.

Tikhale limodzi pamene mphunzitsi wathu akuyamba kutambasula phunziro lathu la lero, lomwe mutu wake ndi **Panalibetu Malo Akubisalapoa**

Insert: Speaker

Pali zinthu/nyengo zingapo mmoyo uno zimene sitimakhala ndi ulamuliro pa machitidwe ake, ndipo chimodzi mwa zinthu zimenezi ndicho kubadwa kwathu. Sitimakhala ndi ulamuliro pa nthawi kapena malo amene ife tinabadwira. Chinthu chinanso chimene tilibe ulamuliro pa icho ndi nyengo. Zivomezi zimadza ndipo palibe angathe kuziletsa. Anamondwe ndi mphepo za mkuntho zimadza ndipo timangokhala kakasi posakhala ndi njira yakuziletsa zinthu zimenezi, chifukwa tilibe ulamuliro pa izo.

Izo zili choncho, mkati mwathu tili nawo ulamuliro wina pa zinthu zina za mmoyo wathu kungoti nthawi zina timayesera kubisa chenicheni chimene tili. Kugulu timaonetsera chithunzithunzi chathu koma chabodza. Koma pamaso pa Mulungu chilichonse chimene tili chimakhala poyera. Mu Salimo 139 zatsimikiziridwa momveka bwino kuti Mulungu ali paliponse ndipo Iye amadziwa kanthu kena kalikonse. Choncho sitingathe kumubisila kanthu

kalikonse. Ndipo pakutero tikuyenera kudziwa choyenera kuchita pamene zili chonchi kuti KULIBE MALO AKUBISALAPO.

Mneneri amene anatumidwa kukakonza njira ya utumiki wa Yesu anapatsidwiratu chithunzithunzi cha zosowa za mbadwo umene adzautumikirawo. Pa Mateyu 3:7-12, tikumva mtumiki ameneyu ali kulankhula ndikuonanso kuti sanawasiyira anthu amene anali kumvera uthenga wake malo akubisalapo.

7Ndipo iye pakuona ambiri a Afarisi ndi a Asaduki akudza ku ubatizo wace, anati kwa iwo, Obadwa a njoka inu, ndani anakulangizani kuthawa mkwiyo ulinkudza? 8Onetsani inu zipatso zakuyenera kutembenuka mtima: 9ndipo musamayesa kunena mwa inu nokha, Atate wathu tiri naye Abrahamu; pakuti ndinena kwa inu kuti mwa miyala iyi Mulungu akhoza kuukitsira Abrahamu ana. 10Ndiponso tsopano lino nkhwangwa yaikidwa pa mizu ya mitengo; cifukwa cace mtengo uli wonse wosabala zipatso zabwino udulidwa nuponyedwa pamoto, 11Inetu ndikubatizani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima; koma Iye wakudza pambuyo panga, ali wakundiposa mphamvu, amene sindiyenera kunyamula nsapato zace: Iyeyu adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto: 12couluzira cace ciri m'dzanja lace, ndipo adzayeretsa padwale pace; ndipo adzasonkhanitsa tirigu wace m'ciruli, koma mankhusu adzatentha ndi moto wosazima.

Mlaliki ameneyu, Yohane m’batizi, anagwedeza mitima ya anthu ndi mfundo zake zamphamvu ndi zopyoza mtima kotero kuti anthu onse akumumvera iye sanatha kupeza malo akubisala.

Mfundo yake yoyamba inakhudza nkhani yakuonetsera zipatso. Ananena ichi pakuona kuti anthuwo anali ndichipembedzo chopanda chilungamo, mawu a choonadi kapena chiphunzitso chenicheni. Anali nacho chipembedzo chofotokozedwa bwino ndipo izi ndi zabwinobwino, chonde mundimvetsetse. Koma munthu sangakhale moyo woyera ngati ali ndi chiphunzitso cholakwika. Choncho kunali kofunikira kuti iwo akhale ndi kumvetsetsa kwa zinthu zonse zofotokozedwa bwino lomwe.

Komabe ntchito za munthu sizingabise chomwe iye ali mkati mwake. Ndipo nzotheka kukhala ndi chipembedzo koma ulibe chidziwitso cha choonadi. Nzothekanso kukhala ndi chipembedzo koma popanda moyo wweniweni wa umulungu. Chipembedzo chopanda ungwiro ndipachabe. Choncho pamene anthuwa anadza kwa Yohane m’batizi, iye anaona mmene iwo analili mkati mwawo, ndipo anati, “Onetsani zipatso zakulapadi!” Chimene munthu ali mkati mwake ndicho zenizeni za moyo wake komanso chinthu chofunikira kwambiri. Iye anali kuwauza kuti chimene munthu uli mkati mwako momwe munthu wina aliyense sangaone koma Mulungu yekha, chimenecho ndiye chenicheni chimene munthu uli.

Ndipo anawatcha iwo ana a njoka, mbadwo wa njoka, njoka zaululu/mphiri. Apatu anali kulozera ku chinyengo cha njoka ija mmunda wa Edeni. Ndikuganiza kuti nkhani imene ija ndi imene anali kutanthauza. Chifukwa pa nkhani imeneyo, tikaiwerenga mu bukhu la Genesis, tidzazindikira mmene njoka inamnyengera mai Hava.

Moyo wokhala mkati mwa munthu umenewo ndiye phata la moyo. Choncho anali kuwachondelera kuti achitepo kanthu pachimenecho. Nzosatheka kuti umunthu wa kunja ukachite/kukwaniritsa zimene umunthu wamkati walephera kubadwitsa. Kulibe malo akubisalirapo pamaso pa Mulungu.

Mfundo yake yachiwiri inakhudza pa nkhani ya banja limene munthu amabadwirako. Pakuti iye anati, “Mumanena mwa inu nokha kuti atate wathu tiri naye Abrahamu.” Musamayesa choncho. Nzoona kuti Abrahamu, amene anakhala moyo wachikhulupiriro ndi wodalira Mulungu, anali

tate wopambana. Tsiku lina usiku Mulungu anamutengera iye kunja kumuonetsa mlengalenga pamene iye anali kukaika. Mulungu anamtengera iye kunja namuonetsa nyenyezi nati kwa iye, “Motero zidzakhala mbewu zako.” Ndipo Abrahamu anakhulupirira Mulungu, anadalira Mulungu. Iye anali tate wopambana chifukwa anakhala moyo wachikhulupiriro ndi kudalira (Mulungu).

Abrahamu anali tate wopambana chifukwa anamvera Mulungu. Pamene Mulungu anamuuza kutenga mwana wake yekhayo, Isaki, ndikukampereka monga nsembe pa phiri la Moriya, Abrahamu anamvera. Baibulo limatiuza kuti iye anatenga mwana wake, Isaki, namuka kuphiri la Moriya ndicholinga chakumpereka iye monga nsembe koma Mulungu anagwira dzanja lake namubweza kuti asatero. Mwaichi Abrahamu anali tate wodabwitsa.

Ndipo Mulungu anadziwa kuti Abrahamu adzalamulira bwino ana ake onse. Koma anawo anali kungonyadira kokha kuti Abrahamu ndiye tate wawo koma sanali kukhala moyo wopambana monga Abrahamu anachitira. Kumbukirani kuti Mulungu sakhala ndi zidzukulu. Aliyense amadziyankhira yekha zochita zake pamaso pa Mulungu. Kubadwira banja lakutilakuti ndi chinthu chofunika koma izi sizingachotse udindo/kufunika kokhala ndimoyo wangwiro/wachikhulupiriro.

Yohane m’batizi ananena kuti mtengo uliwonse woipa udzadulidwa basi. Nkhwangwa yasamulidwa kale, kulunjika ku muzu wamtengo chifukwa mtengo ngosabala chipatso chabwino, choncho udulidwa ndikutayidwa ku moto. Mulungu akudziwa mmene inu mukhonza kumakhulupirira zoti munabadwira kumtundu/banja lopambana pa zachipembedzo. Koma mtundu wa banja lomwe mumachokera sungapezetse malo pamaso pa Mulungu pokhapokha mutadzilumikizitsa nokha ndi Mulunguyo.

Mfundo yake yachitatu inakhudza pa nkhani ya malire/polekezera pake. Munthu ali ndi malire. Choncho Yohane analinso ndi polekezera. Iye anawaonetsera anthuwo kuti iye akhonza kuchitapo zinthu koma monga munthu udindo wake ukhonza kukhala ndi polekezera. Ndipo iye anawaitanira ku kutembenuka mtima nawabatiza iwo ndi madzi kusonyeza kulapa. Koma pamenepa mpamene Yohane analekezera.

Nkofunika kuzindikira kuti munthu ali ndi malire, ndipo Yohane anadziwa izi. Kotero kuti anadziwa zokhazo zomwe utumiki wake ukanakwanitsa kuzichita ndizo kuitanira anthu kukulapa ndi kuwapatsa ubatizo wosonyeza kulapa kwawo. Koma iye anati kuweruza/kusiyanitsa kwenikweni kudzaoneka wamkulukuluyo akadzabwera. Pakuti iye anati, “Iye wakudza pambuyo panga ali wamphamvu kuposa ine, ndipo Iye adzalekanitsa mankhusu kuwachotsa pakati pa tirigu. Ndipo adzabatiza anthu ndi Mzimu Woyera komanso moto, ndipo mdzanja lake muli chowuluzira chakulekanitsa tirigu ndi mankhusu. Tirigu adzamuika mu nkhokwe yake koma mankhusu onse adzawatentha ndi moto wosazimitsika.”

Izi ndi mfundo zodabwitsa zimene Yohane m’batizi anali kutsogozedwa nazo. Anaona kuti padzakhala polekezera pamene wina aliyense sangadutsepo. Panali polekezera pa zomwe akanachita mu utumiki wake ndikutinso kulekanitsa kumene Wakumuposa mphamvu adzakwaniritse akadzabwera. Kotero kuti zotsatira zomaliza zili mmanja ndi ulamuliro wa Wamphamvu zoposayo.

Insert: Signtune 10 Secs

Presenter :

Apatu ndiye pamapeto pa Phunziro lathu la lero, pamene wotiphunzitsa amasanthula pamutu woti, **Panalibetu Malo Akubisalapoa**

. Kufikira utumiki wa Heralds of Hope utatipatsira phunziro lina, mu programu inanso, tiyeni tipitilize kufunafuna chiyembekezo chodala.